

CHIKHULUPIRIRO CHA AKHRISTU



1. Ndikhulupirira Mulungu Atate, Wamphamvuyonse, Wolenga zakumwamba ndi zapansi;
2. Ndikhulupirira Yesu Khristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu;
3. Amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa mwa Mariya namwaliyo;
4. Nasautsidwa kwa Pontio Pilato; napachikidwa pamtanda, nafa, naikidwa m'manda, natsikira kwa akufa;
5. Tsiku lachitatu anaukansa kwa akufa;
6. Nakwera kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate Wamphamvuyonse;
7. Kudzera komweko adzadza kudzaweruzza anthu amoyo ndi akufa;
8. Ndikhulupirira Mzimu Woyera;
9. Ndkhulupirira Mpingo Wopatulika wa Khristu, wa kwa anthu onse, chijanano cha oyera mtima mtima;
10. Kukhululukidwa kwa machimo;
11. Kuukansa kwa thupi;
12. Ndi moyo wosatha. AMEN.

MALAMULO KHUMI

1. Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndekha.
2. Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena chifaniziro chirichonse cha zinthu za m'thambo la kumwamba kapena kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansu pa dziko.
3. Usatchule dzina la Yehova Mulungu wako pachabe.
4. Udzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika.
5. Uzilemekeza atate wako ndi amako, kuti achuluke masiku ako m'dziko limene Yehova Mulungu wako akupatsa iwe.
6. Usaphe.
7. Usachite Chigololo.
8. Usabe.
9. Usamnamizire mnzako.
10. Usasirire.

PEMPHERO LA AMBUYE

Atate wathu wakumwamba:

Dzina Lanu liyeretsedwe;

Ufumu Wanu udze;

Kufuna kwanu kuchitidwe;

Monga kumwamba;

Chomwecho pansu pano.

Mutipatse ife lero;

Chakudya chathu chalero.

Ndipo mutikhululukire zochimwa zathu;

Monga ifenso tiwakhululukira amangawa athu.

Musatitengere ife kokatiyetsa;

Koma mutipulumutse ife kwa oipayo.

Chifukwa wanu ndi Ufumu, ndi Mphamvu, ndi Ulemerero wa nthawi zonse. AMEN.

MAU OYAMBILIRA

Abale ndi alongo mwa Ambuye. Katikisimu ndi buku mmene malangizo ake kapena chiphunzitso chake chimakhala ndi funso komanso yankho. Buku ili likutchedwa Katekisimu Wachidule kuti asiyanitsidwe ndi wina wankulu amene mafunsowa atanthauziridwa kwambiri. Katekisimuyi analembedwa mchaka cha 1647 ndi abusa osiyanasiyana ndi atsogoleri ena amene anasonkhana pa malo otchedwa Westminster, omwe ali mu Mzinda uja wotchuka wa London ku Magalande. Abusawatu amakonza madziko a mpingo wamoyo wa Ufumu Wa Mulungu. Katekisimu ali ndi mafunso komanso mayankho okwana 107. Mafunso oyambilira atatu ndi ongotitsogolera. Kenako pali mafunso 33 (kuchokera funso 4 mpaka 38). Mafunso 33 amenewa amatiuza zimene ife tiyenera kukhulupirira. Mafunso ena onse otsalawo omwe ndi 69 (funso 39 mpaka 107) amatiuza zimene ife tiyenera kumachita.

Bukuli ndi lofunika kwambiri kwa Mkhristu aliyense chifukwa mafunso onse 107 amangika pa madziko a Chikhristu. M'buku ili mafunsowa agawidwa m'magawo aafupi kuti munthu wowerenga ndi wophunzira bukuli athe kutsatira bwino.

Mubulinso muli mavesi a m'Baibulo amene akuperekera umboni wa funso liri lonse ndipo kutsimikizira kuti mayankho onsewa achokera mu Buku limeneli lomwe ndi Lopatulika chifukwa ndi Mau A Mulungu.

Kumapeto a bukuli taikanso mafunso onse 107 ngati kubwereza kuti owerenga aonesetse kuti akutsatiradi ndipo ngati nkotheke kuloweza mafunso ndi mayankho onse. Kumayambiliro monga mmene mwaonera mulinso Chikhulupiro cha Akhristu, Malamulo Khumi, komanso Pemphero La Ambuye zimene Akhristu a Evangelical Presbyterian Church ayenera kuloweza pamtima.

Ambuye akudalitseni nonse pamene muli pa ntchito yotamandika ngati imeneyi yowerenga ndi kuloweza Katekisimuyi kuti moyo wanu wa uzimu upite patsogolo zimenenso zipangitse kuti mpingo wathu upite patsogolo.

Rev. Rex Chitekwe

M'malo mwa Evangelical Presbyterian Church Synod Executive Committee

May, 2012

KATEKISIMU WACHIDULE WA WESTMINSTER

FUNSO 1. Kodi cholinga chenicheni chimene munthu ayenera kuchita kwa Mulungu ndi chiyani?

YANKHO. Cholinga chenicheni chimene munthu ayenera kuchita ndiko kulemekeza Mulungu ndi kukondwerera mwa Iye nthawi zonse.

1 Akorinto 10:31; “chifukwa chake mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena, chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu”. Masalimo 73:25-26; “Ndiri ndi yani kumwamba koma Inu? Ndipo padziko lapansi palibe wina wondikonda koma Inu. Likatha thupi langa ndi mtima wanga: Mulungu ndiye thanthwe la mtima wanga, ndi chodalira change chosatha”.

FUNSO 2. Kodi ndi lamulo liti lomwe Mulungu wapereka lotitsogolera ife m’menetingamlemekezere ndi kukondwerera mwa Iye?

YANKHO. Mawu a Mulungu amene ali m’Chipangano Chakale ndi Chatsopano ndi okhawo amene ali lamulo lotitsogolera ife m’mene tingamlemekezere ndi kukondwera mwa Iye.

Aefeso 2:20; “Omangika padziko atumwi ndi aneneri pali Khristu Yesu mwini, mwala wa pangodya”. 2 Petro 3:7; “Koma miyamba ndi dziko la masiku ano, ndi mawu omwewo zaikika kumoto, zasungika kufikira tsiku la chiweruzo ndi chiwonongeko cha anthu osapembedza”. 2 Timothy 3:16; “Lemba lililonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitsa, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha nchilungamo”.

FUNSO 3. Kodi mawu a Mulungu kwenikweni amaphunzitsa chiyani?

YANKHO. Mawu a Mulungu kwenikweni amaphunzitsa chimene munthu ayenera kukhulupirira chokhuza Mulungu, ndi udindo wa munthu kwa Mulungu.

2 Timoteo 1:13; “Gwira chitsanzo cha mawu a moyo, amene udawamva kwa ine, mwa chikhulupiliro ndi chikondi chili mwa Khristu Yesu”.

GAWO LOYAMBA :ZIMENE TIYENERA KUKHULUPIRIRA

1. M’MENE MULUNGU ALILI

FUNSO 4. Kodi Mulungu ndi ndani?

YANKHO. Mulungu ndi Mzimu, Wopanda malire, wamuyaya ndi wosasinthika, mu kukhala kwake, mu nzeru, mu mphamvu, mu chiyero, mu chilungamo, mu ubwino ndipo muchoonadi chake.

Yohane 4:24; “Mulungu ndiye Mzimu, ndipo omulambira Iye amulambire mu Mzimu ndi mchoonadi”. Yobu 11:7 “Kodi ukhoza kupeza Mulungu mwa kufunafuna? Ukhoza kupeza wamphamvu yonse motsindika”? Masalimo 90:2; “Asanabadwe mapiri, kapena musanalenge dziko lapansi, ndi lokhalamo anthu, Inde, kuyambira nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha, Inu ndinu Mulungu”.

FUNSO 5. Kodi ilipo Milungu inanso?

YANKHO. Pali Mulungu m’modzi yekha, wa moyo ndi woona.

Deuteronomo 6:4; “Imvani, Israeli Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye m’modzi”. Yeremiya 10:10; “Koma Yehova ndiye Mulungu woona, ndiye Mulungu wamoyo, Mfumu yamuyaya; pa mkwiyo wake wa dziko lapansi lidzanthunthumira ndi amitundu sangapilire ukali wake”.

FUNSO 6. Kodi mu Umulungu muli anthu angati?

YANKHO. Mu Umulungu muli anthu atatu: Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Ndipo atatuwa ali Mulungu m’modzi, ofanana muchikhalidwe, mu mphamvu ndi mu ulemerero.

Mateyu 28:19; “Chifukwa chake mukani phunzitsani anthu amitundu yonse ndi kuwabatiza iwo m’dzina la Atate, ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera”. 1 Yohane 5:7; “Ndipo Mzimu ndiye wakuchita umboni chifukwa Mzimu ndiye choonadi”.

2. ZIMENE MULUNGU WACHITA

FUNSO 7. Kodi malamulo a Mulungu ndi otani?

YANKHO. Zolinga za Mulungu zili zosatha molingana ndi uphungu wa chifuniro chake kotero kutimwaulemerero wake lye anakonzeratu zinthu zinse zochitika.

Aefeso 1:11-12; “Mwa lye tinayesedwa cholowa chake, popeza tinakonzekeratu monga mwa chitsimikizo mtima chake lye wakuchita zonse monga uphungu wa chifuniro chake; kuti ife tikayamikitse ulemerero wake”.

FUNSO 8. Nanga Mulungu akukwaniritsa bwanji malamulo ake?

YANKHO. Mulungu akukwaniritsa malamulo ake muntchito zachilengedwe ndi muchisamaliro.

Chibvumbulutso 4:11; “Muyenera Inu Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, Kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu; chifukwa mudalenga zonse, ndipo mwa chifuniro chanu zinakhala Ndipo zinalengedwa”. Danieli 4:35; “Ndi okhala padziko onse ayesedwa achabe, ndipo lye achita mwa chifuniro chake m’khamu lakumwamba ndi mwa okhala pa dziko lapansi; ndipo palibe woletsa dzanja lake, kapena wakunena naye muchitanji?”

3. CHILENGEDWE

FUNSO 9. Kodi ntchito ya chilengedwe ndi yotani?

YANKHO. Ntchito ya chilengedwe ndiko kupangidwa kwa zinthu zonse ndi Mulungu kuchokerapopanda kanthu, mu mphamvu ya mawu ake m’masiku asanu ndi limodzi ndipo zonse zinali bwino.

Genesis 1:1; “Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi”. Ahebrei 11:3; “Ndi chikhulupiriro tizindikira kuti maiko onse, ndi a m’mwamba omwe anakonzedwa ndi mawu a Mulungu, kotero kuti zinthu zopenyeka sizinapangidwa zochokera mwa zoonekazo”. Genesis 1:31; “Ndipo adaziwona Mulungu zonse zimene adazipanga ndipo taonani, zinali zabwino ndithu. Ndipo panali madzulo ndipo panali m’mawa, tsiku lachisanu ndi chimodzi”.

FUNSO 10. Kodi munthu analengedwa bwanji?

YANKHO. Mulungu analenga munthu, mwamuna ndi mkazi mu chifaniziro chake, muchidziwitso, m’chilungamo ndi m’chiyero ndikuti alamulire pazolengedwa zonse.

Genesis 1:27; “Mulungu ndipo adalenga munthu muchifanizo chake, muchifanizo cha Mulungu adamulenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi”. Genesis 1:28; “Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, mubalane muchuluke, mudzadze dziko lapansi, muligonjetse; mulumulire pa nsomba za mnyanja ndi mbalame pa mlengalenga ndi pa zonse za moyo zakukwawa pa dziko lapansi”.

4. NTCHITO ZA MULUNGU MU CHISAMALIRO CHAKE

FUNSO 11. Kodi ntchito za Mulungu muchisamaliro chake ndi zotani?

YANKHO. Ntchito za Mulungu muchisamaliro chake ndi chiyero chake, nzeru zake ndi mphamvuyakusunga ndi kulumulira zolengedwa zake ndi zichitochito zawo.

Masalimo 145:17; “Yehova ali wolungama m’njira zake zonse. Ndi wachifundo m’ntchito zake zonse”. Yesaya 28:29; “Ichinso chifumira kwa Yehova wa makamu, uphungu wake uzizwitsa ndi nzeru yake ipambana”.

FUNSO 12. Kodi ndi chisamaliro chapadera chotani chimene Mulungu anaonetsera kwa munthu m’munda umene analengedwera?

YANKHO. Pamene Mulungu analenga munthu, munthuyo analowa mu chipangano cha moyo ndi iye pakulonjeza. kumvera kwa ngwiro; kumuletsa iye kudya chipatso cha mtengowodziwitsa zabwino ndi zoipa umene unali ndi ululu wa imfa.

Agalatiya 3:12, “Koma chilamulo sichichokera ku chikhulupiriro; koma wakuzichita izi adzakhala ndi moyo ndi izi”. Genesis 2:17, “koma mtengo

wakudziwitsa zabwino ndi zoipa usadye, chifukwa tsiku limene udzadye udzafa ndithu” .

5. MMENE MUNTHU ANACHIMWIRA

FUNSO 13. Kodi makolo anthu oyamba anapitilira kukhalabe m'mene adalengedwera?

YANKHO. Makolo athu oyamba popatsidwa ululu wa chifuniro cha iwo eni, anagwa ndi kuchokammene analengelengedwera ndi Mulungu.

Deutronomo 30:19; “Ndichititsa mboni lero kumwamba ndi dziko lapansi zitsutse inu; ndaika pakati panu moyo ndi imfa, mdalitso ndi temberero; potero sankhani moyo kuti mukhale ndi moyo, inu ndi mbeu zanu”. Mlaliki 7: 29, “Taonani ichi chokha ndachipeza kuti Mulungu analenga anthu oongoka mtima; koma iwowa anafunafuna malongosedwe a mitundu mitundu”.

FUNSO 14. Kodi tchimo ndi chiyani?

YANKHO. Tchimo ndi kulephera kuchita chifuniro cha Mulungu kapena kuphwanya malamulo aMulungu.

Luka 10: 31; “Ndipo kudangotero kuti wansembe wina anatsika njirayo, ndipo pakumuona iye anapita mbali yina”. Luka 22:61; “Ndipo Ambuye anapotoloka, nayang’ana Petro. Ndipo Petro akumbukila mau a Ambuye, kuti anati kwa iye, asanalire tambala lero lino, udzandikana lne katatu”.

FUNSO 15. Kodi ndi tchimo lanji limene linapangitsa makolo athu oyamba kugwa kuchokera m’manja mwa Mulungu?

YANKHO. Tchimo limene linapangitsa makolo athu oyamba kugwa kuchokera m’manja mwaMulungu ndilo kudya chipatso choletsedwa.

Genesis 3: 6-8; “Ndipo pamene anaona mkaziyo kuti mtengo unali wabwino kudya, ndi kuti unali wokoma m’maso, mtengo wolakalakika wakupatsa nzeru, anatenga zipatso zake, nadya, napatsanso mwamuna wake amene anali naye, nadya iyenso”.

6. ZOTSATIRA ZAKUCHIMWA KWA MUNTHU

FUNSO 16. Kodi mtundu wonse wa anthu unachimwanso pamene Adamu anachimwakoyamba?

YANKHO. Pokhala chipangano chinachitika pakati pa Mulungu ndi Adamu, osati kwa iye yekhakomanso ndi mbewu yake, mtundu wa anthu onse ochokera mwa iye monga mwamibadwo, anachimwa naye limodzi mu tchimo lake loyamba.

Aroma 5: 18, 19; “Chifukwa chake, monga mwa kulakwa kumodzi kutsutsa kunafikira anthu onse; chomwechonso . Pakuti monga ndikusamvera kwa munthu mmodzi ambiri anayesedwa ochimwa”. 1 Akorinto 15: 22; “Pakuti monga mwa Adamu onse amwalira, choteronso mwa Khristu onse akhalitsidwa ndi moyo”.

FUNSO 17. Nanga kugwa kwa Adamu kunabweretsa chiyani ku mtundu wa anthu?

YANKHO. Kugwa kwa Adamu kunabweretsa tchimo ndi mazunzo ku mtundu wa anthu.

Aroma 5:12; “Chifukwa chake monga uchimo unalowa m’dziko mwa munthu m’modzi ndi imfa mwa uchimo; koteronso imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa”.

FUNSO 18. Kodi tchimo limene linafikira munthu limapezeka mu chiyani?

YANKHO. Uchimo umenewu unapezeka mu tchimo la Adamu, mukuperewera kwa chilungamochapachiyambi, komanso kuonongeka kwa chikhaldwe chake chonse, kumene kumatchedwa tchimo lapachiyambi, pamodzi ndi zonse zotuluka mmenemo.

Aroma 5:19; “Pakuti monga ndi kusamvera kwa munthu m’modzi ambiri anayesedwa ochimwa”. Masalimo 51:5; “Onani ndinabadwa mphulupulu ndipo amayi wanga anandilandira m’zoipa”.

FUNSO 19. Kodi ndi masautso otani amene anabwera kwa munthu chifukwa cha uchimo?

YANKHO. Mtundu wonse wa anthu unataya chiyanjano ndi Mulungu chifukwa cha uchimo ndipo iwo uli pansi pa mkwiyo ndi temberero lake ndi kuwabweretsera masautso a moyo uno, a imfa, ndi zowawa za ku gahena kunthawi zosatha.

Yesaya 59:2; “Koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo machimo anu abisa nkhope yake kwa inu, kuti lye sakumva. Ezekiel 18:4; “Moyo wochimwawo ndiwo udzafa”.

7. CHIPULUMUTSO

FUNSO 20. Kodi Mulungu analekelera mtundu wa anthu kuti uwonongeke m’machimo ndi m’masautso awo?

YANKHO. Popeza chifuniro cha Mulungu ndi chabwino, anasankha ena ku moyo wosatha kulowa nawo mu Pangano la Chisomo, pa kuwavuula mu uchimo ndi m’ mavuto ndi kuwayika iwo m’chiwombolo chochitidwa ndi MPULUMUTSI.

Genesis 3:15; “Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yake; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira chitende chake. 2 Timoteo 1:9; “ Amene anatipulumutsa ife, natiitana ndi maitanidwe oyera, simonga ndi ntchito zathu, komatu monga mwa chitsimikizo mtima cha lye yekha, ndi chisomo, chopatsika kwa ife mwa Khristu Yesu zisanayambe nthawi zoyamba”.

FUNSO 21. Kodi Mpulumutsi wa anthu osankhidwa a Mulungu ndi ndani?

YANKHO. Mpulumutsi wa osankhidwa a Mulungu ndi Ambuye Yesu Khristu, amene pokhala Mwana wa Mulungu, ANASANDUKA MUNTHU, ndipo anakhalabe , ndipo akupitirizakukhala, MULLUNGU NDI MUNTHU, kwa muyaya.

Machitidwe 4:12; “Ndipo palibe chipulumutso mwa wina aliyense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo”. Ahebr 2:

14; “Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, lyenso momwemo adalawa nao makhalidwe omwewo kuti mwa imfa akamuononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi”.

FUNSO 22. Kodi Khristu pokhala mwana wa Mulungu anakhala bwanji munthu?

YANKHO. Khristu Mwana wa Mulungu anakhala munthu pakudzitengera kwa lye Yekha THUPILENILENI, NDI MOYO ndi kubadwa mwa namwali Mariya kupyolera mu mphamvu ya Mzimu ndipo anabadwa opanda tchimo.

Luka 1:35; “Ndipo mngelo anayankha, nati kwa iye, Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya wamkulukulu idzakuphimba iwe: chifukwa chakenso Choyeracho chikadzabadwa, chidzachedwa Mwana wa Mulungu”. Agalatiya 4:4; “Koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu anatuma Mwana wake wobadwa ndi mkazi, wobadwa wakumvera lamulo”.

8. NTCHITO YA YESU MU CHIPULUMUTSO

FUNSO 23. Kodi ndi mauidindo ati amene Khristu ali nawo monga mombolo wathu?

YANKHO. Khristu monga mombolo wathu akugwira ntchito yake monga MNENERI, WANSEMBE komanso MFUMU, muchikhalidwe chake CHODZICHEPETSA komanso mu ULEMELERO.

Machitidwe 3: 22; “Mosetu anati, Mbuye Mulungu adzaukitsira inu mneneri mwa abale anu, ngati ine; mudzamvera iye m’zinthu ziri zonse akalankhule nanu.” Ahebr 5:6; “Monga anananso mwina, lwe ndiwe wansembe wa nthawi zonse Monga mwa dongosolo la Melikizedeke”. Masalimo 2:6 “Koma ine ndadzoza mfumu yanga Pa Ziyoni, phiri langa loyera”.

FUNSO 24. Kodi Khristu akugwira bwanji ntchito yake ya Uneneri?

YANKHO. Khristu akugwira ntchito yake ya uneneri pakuti ululira ife kupyolera mu mau ake ndi Mzimu Woyera mu CHIFUNIRO CHAMULUNGU zokhuza chipulumutso Chathu.

Yohane 16:13; Koma atadza lyeyo, Mzimu wa choonadi, adzatsogolera inu m'choonadi chonse; pakuti sadzalankhula za lye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirikudza adzakulalikirani". Ahebr 1: 1, 2; "Kale Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyana-siyana, koma pakutha pake pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse mwa lyenso analenga maiko ndi a m'mwamba omwe".

FUNSO 25. Kodi Khristu amagwira bwanji ntchito yake ya unsembe?

YANKHO. Khristu amagwira ntchito yake monga wansembe pakuzipereka kwake NSEMBE pokwaniritsa chilungamo cha u Mulungu ndi kutiyanjanitsa ife ndi Mulungu, komanso kutipembezero ife ife kosalekeza.

Ahebr 4: 14; "Popeza tiri naye Mkulu wansembe wamkuru, wopyoza miyamba, Yesu mwana wa Mulungu, tigwiritsitse chivomerezo chathu. Ahebr 9:28; "Kotero Khristunso ataperekedwa nsembe kamodzi kukasenza machimo a ambiri, adzaonekera pa nthawi yachiwiri, wopanda uchimo, kwa iwo amene amlindirira, kufikira chipulumutso. Akolose 1:20; "Mwa lyenso kuyanjanitsa zinthu zonse kwa lye mwini, atachita mtendere wa mtanda wake; mwa lyetu, kapena za padziko, kapena za m'mwamba".

FUNSO 26. Nanga Khristu anakwaniritsa bwanji udindo wake monga mfumu?

YANKHO. Khristu anakwaniritsa udindo wake monga mfumu potikekera ife kwa lye yekha, pakulamulira ndi kutiteteza, kutigwiritsa ndi kugonjetsa adani athu ndi ake.

Masalimo 110:3 "Anthu anu adzadzipereka eni ake tsiku la chamuna chunu: m'moyera mokometsetsa, mobadwira m'bandakucha, muli nao mame a ubwana wanu." Yesaya 33: 22 "Pakuti Yehova ndiye woweruza wathu, Yehova ndiye wotipatsa malamulo, Yehova ndiye Mfumu yathu ya lye adzatipulumutsa". 1 Akorinto 15:25, "Pakuti ayenera kuchita ufumu, kufikira ataika adani onse pansu pa mapazi ake".

FUNSO 27. Kodi kudzichepetsa kwa Khristu kunali kotani?

YANKHO. Kudzichepetsa kwake kwa Khristu kunaonekera m'kubadwa kwake mnjira yodzichepetsa mwa lamulo podutsa mmavuto a moyo uno, mu mkwiyo wa Mulungu ndi temberero la imfa ya pamtanda, ndikuikidwa m'manda ndikukhala pansu pa mphamvu ya imfa kwakanthawi.

Luka 2:7; "Ndipo lye anabala mwana wake wa mwamuna woyamba; namkulunga lye m'salu nam'goneka modyera ng'ombe, chifukwa kuti anasowa malo mnyumba ya alendo". Agalatiya 4:4; Koma pokwaniridwa nthawi Mulungu anatuma Mwana wake wobadwa ndi mkazi, wobadwa wakumvera lamulo" Yesaya 53:3; "Iye ananyozedwa ndikukanidwa ndi anthu, munthu wazisoni, ndi wodziwa zowawa; ndipo ananyozedwa monga munthu wobisira anthu nkhope zawo; ndipo ife sitinamulemekeza'.

FUNSO 28. Kodi kupambana kwa Yesu kunali kotani?

YANKHO. Kupambana kwa Yesu kunali pakuuuka kwa akufa patsiku lachitatu ndi kukweranso kumwamba, ndikukhala kudzanja la manja la Mulungu Atate ndikubweranso kudzaweruza dziko lonse lapansi pa tsiku lotsiriza.

1 Akorinto 15:4; "Ndikuti anaikiidwa, ndikuti anaukitsidwa tsiku lachitatu monga mwa malembo". Marko 16:19; "Pamenepo Ambuye Yesu atatha kulankhula nawo analandiridwa kumwamba nakhala padzanja lamanja la Mulungu". Machitidwe 17:31; "Chifukwa anapangira tsiku limene adzaweruza dziko lokhalamo anthu m'chilungamo, ndi munthu amene anamuikiratu; napatsa anthu onse chitsimikizo, pamene anamuukitsa lye kwa akufa'.

9. NTCHITO YA MZIMU MU CHIPULUMUTSO

FUNSO 29. Kodi timatenga nawo gawo bwanji ku chiwombolo chimene Khristuanatibweretsera?

YANKHO. Ife timatenga nawo gawo kuchiwombolochi pamene Mzimu wake Woyera akhalamwa ife.

Yohane 1:12; “Koma onse amene anamulandira Iye, anapatsa mphamvu kwa iwo yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu akukhulupirira dzina lake”. Tito 3: 5,6; “Zosati zochokera ntchito za chilungamo zimene tidachita ife, koma monga mwa chifundo chake anatipulumutsa ife, mwakutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera, amene anatsanulira pa ife mochulukira mwa yesu Khristu Mplumutsi wathu’.

FUNSO 30. Kodi Mzimu Woyera amatibweretsera bwanji chiwombolo cha Khristu?

YANKHO. Mzimu Woyera amatibweretsera chiwombolo cha Khristu kupyolera mu chikhulupiriro cha ntchito cha mwa ife, kutiluzanitsa ife kwa Khristu mmaitanidwe athu.

Aefeso 2:8; “Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwachikulupiriro, ndipo ichi ndi chosachokera kwa inu chili mphatso ya Mulungu”. Aefeso 3:17; “Kuti Khristu akhale chikhaliye m’mitima yanu; kuti ozika mizu, ndi otsendereka mchikondi”. 1 Akorinto 1:9; “Mulungu ali okhulupirika amene munaitanidwa kwa Iye, kuchiyanjano cha Mwana wake Yesu Khristu, Ambuye wathu”.

FUNSO 31. Kodi maitanidwe enieni ndi chiyani?

YANKHO. Maitanidwe enieni ndi ntchito ya Mzimu Woyera wa Mulungu pamene atitsimikizira ife za machimo athu ndi mazunzo pakutiunikira ife m’maganizo, mchidziwitso cha Khristu ndi kukonzanso chifuniro chathu. Iye amatikakamiza ndikutipangitsa ife kufungatira Yesu Khristu wopatsidwa kwa ife mwaulere wa Uthenga Wabwino.

2 Timoteo 1:19; “Amene anatipulumutsa ife natiitana ife ndi maitanidwe oyera, simonga mwa ntchito zathu, komatu monga mwa chitsimikizo mmitima cha Iye Yekha, chi chisomo chopatsika kwa ife mwa Khristu Yesu zisanayambe nthawi zoyamba”. Machitidwe 2: 37; “Koma pamene anamwa ichi, analaswa mtima, natitu kwa Petro ndi atumwi enawo, tidzachita chiyani, amuna inu abale?” Ezekieli 36:26; “Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano ndi kulonga mkati mwanu, ndipo ndidzachotsa mtima wa mwala mthupi ndikukupatsani mtima wa mnofu”. Yohane 6:44-45; “Kulibe m’modzi akhoza kudza kwa Iye, koma ngati Atate wondituma Iye amkoka iye, ndipo Iye ndidzamuukitsa iye tsiku lomaliza. Chalembedwa mwa aneneri, ndipo adzakhala onse ophunzitsidwa ndi Mulungu. Yense amene adamva kwa Atate naphunzira , adza kwa Iye”.

10. PHINDU LA CHIPULUMUTSO M'MOYO UNO

FUNSO 32. Kodi pali phindu lanji limene oitanidwa amapeza mmoyo uno?

YANKHO. Phindu limene iwo amapeza m’moyo uno ndi kulungamitsidwa kukhala Mwana wa Mulungu ndi kuyeretsedwa ndi zina zambiri zabwino zimawatsatira iwo.

Aroma 8:30; “Ndipo amene Iye anawalamuliratu, iwo anawaitananso; ndimo lwo amene Iye anawaitana, iwowa anawayesanso olungama; ndi iwo amene Iye anawayesa olungama, iwowa anawapatsanso ulemmerero”. Aefeso 1:5; “ Pakuti ichi muchidziwe kuti wadama yense kapena wachidetsa kapena wosirira, amene apembedza mafano, alibe cholowa muufumu wa Khristu ndi Mulungu’. 1 Akorinto 1:30; “ Koma kwa Iye muli inu mwa Khristu Yesu, amene anayesedwa kwa ife nzeru ya kwa Mulungu, ndi chilungamo ndi chiyeretso ndi chiwombolo.

FUNSO 33. Kodi kulungamitsidwa ndi chiyani?

YANKHO. Kulungamitsidwa ndi mphamvu ya chisomo chaulere cha Mulungu, imene Iye amatikhululukira machimo athu onse, ndikutiyesa ife olungama pamaso pake mwachilungamo cha Khristu choikidwa mwa ife, ndiponso cholandiridwa mwa chikhulupiriro basi.

Aefeso 1:7; “Tiri ndi maamboledwe mwa mwazi wake, chikhululukiro cha zochimwa monga mwa kulemera kwa chisomo chake”. 2 Akorinto 5:21; “Ameneyo sanadziwa uchimo, anamyeresera uchimo m’malo mwathu; kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu mwa lye”. Aroma 5:19; Pakuti monga ndikusamvera kwa munthu m’modzi ambiri anayesedwa ochimwa, chomwechonso ndikumvera kwa m’modzi onse adzayesedwa olungama”. Agalatiya 2:16; “Koma podziwa kuti munthu sayesedwa olungama pa ntchito ya lamulo koma mwa chikhulupiriro cha Yesu Khristu, ifedi tinakhulupirira kwa yesu Khristu, kuti tikayesedwa olungama ndi ntchito ya lamulo”.

FUNSO 34. Kodi kukhala mwana wa Mulungu kukutanthauza chiyani?

YANKHO. Kukhala mwana wa Mulungu kukutanthauza mphatso yachisomo chaulere cha Mulungu, imene timalandiridwa mgulu la ana a Mulungu ndikukhala ndi ufulu wonse pa cholowa cha ana a Mulungu”.

Yohane 1:12; “Ngati ndakuuzani za pansi pano, ndipo simukhulupirira, mudzakhulupirira bwanji ngati nditakuuzani za kumwamba? Aroma 8:17; “Ndipo ngati ana, pomweponso olowa nyumba; inde olowa anzake a Khristu; ngatitu ife timva zowawa pamodzi naye, kutit tikalandirenso ulemerero pamodzi ndi lye”.

FUNSO 35. Kodi chiyeretso ndi chiyani?

YANKHO. Chiyeretso ndi ntchito ya chisomo chaulere cha Mulungu imene ife timakonzedwanso muchifaniziro cha Mulungu pakufa mu uchimo ndikukhala muchilungamo.

2 Atesalonika 2:13 “Ndipo mwaichinso, ifenso tiyamika Mulungu kosalekeza, kuti pakulandira mawu a Uthenga wa Mulungu, simunawalandira monga mawu a anthu, komatu mawu a Mulungu amenenso achita mwa inu okhulupirira”. Aefeso 4:24; “Nimuvale munthu watsopano, amene analengedwa monga mwa Mulungu, m’chilungamo, ndi m’chiyero cha choonadi”. Aroma 8:1 “Chifukwa chake tsopano iwo akukhala mwa Khristu Yesu alibe kutsutsidwa”.

FUNSO 36. Kodi ndi phindu lanji ku moyo uno limene limabwera chifukwa cha

kulungamitsidwa, kukhala mwana wa Mulungu, ndi kuyeretsedwa?

YANKHO. Ku moyo uno phindu limene limabwera chifukwa cha kulungamitsidwa, kukhala mwana wa Mulungu ndi kuyeretsedwa ndi: Chitsimikizo chachikondi cha Mulungu, mtendere wa chikumbumtima, chimwemwe mwa Mzimu Woyera, kukula mu chisomo ndikukhala wopirira mpaka kumapeto.

Aroma 5: 1, 2, 5; “Popeza tsono tayedwa olungama ndi chikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu wa Ambuye wathu Yesu Khristu, amene ife tikhoza kulowa naye chikhulupiriro mchisomo ichi mmene tirikuimamo; ndipo tikondwera mchiyembekezo cha ulemerero wa Mulungu. Ndipo chiyembekezo sichichititsa manyazi, chifukwa chikondi cha Mulungu chinatsanulidwa m’mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife”. Miyambo 4:18; “Koma mayendedwe a olungama akunga kuunika kwa m’bandakucha, kunkabe kuwala kufikira usana woti mbe”. 1 Yohane 5:13; “Izi ndakulemberani kuti mudziwe kuti tili nazo izi tazipempha kwa lye”.

11. PHINDU LACHIPULUMUTSO UKATHA MOYO UNO

FUNSO 37. Kodi okhulupirira akamwalira amalandira phindu lanji kuchokera kwa Khristu?

YANKHO. Mizimu ya anthu okhulupirira imalungamitsidwa mu chiyero ndipo imalowa mu ulemerero; ndipo matupi awo ali chilumikizire ndi Khristu, amapumula m’manda kufikira kuuka kwa akufa.

Ahebri 12:23; “Ndi kwa msonkhano wa onse ndi Mpingo wa obadwa olembedwa oyamba olembedwa m’mwamba ndi kwa Mulungu Woweruza wa onse, ndi kwa angwiro”. Afilipi 1:23; “Koma ndipaniidwa nazo ziwiri, pokhala nacho cholakalaka chakuchoka kukhala ndi Khristu ndiko kwabwino kopoulosu”. 1 Atesalonika 4:14; “Pakuti ngati tikhulupirira kuti Yesu adamwalira, nauka koteronso Mulungu adzatenga pamodzi ndi lye iwo akugona mwa Yesu”. Yesaya 57: 2; “Iye alowa mu mtendere, iwo apuma pa mphasa zawo, yense woyenda moongoka”. Yobu 19:26; “Ndipo khungu

langa litaononongeka, pamenepo wopanda thupi langa, ndidzapenya Mulungu”.

FUNSO 38. Kodi ndi phindu lanji limene okhulupirira adzalandira pa tsiku lamdzukiro?

YANKHO. Pa mdzukiro okhulupirira adzaukitsidwa kunka ku ulemerero nadzavomerezidwa poyera ndikuweruzidwa monga anthu osachimwa ndipo adzakhala mu mdalitso ndi muchikondwerero chachikulu cha Mulungu ku nthawi zonse.

1 Akorinto 15:43; “Lifesedwa m’mnyozo liukitsidwa m’ulemerero; liukitsidwa mu mphamvu”. Mateyu 10:32; “Chifukwa chake yense amene adzavomereza Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzavomereza iye pamaso pa Atate wanga wa kumwamba”. 1 Yohane 3:2; “Kuti mukumbukire mawu onenedwa kale ndi aneneri oyera ndi lamulo la Ambuye ndi Mpulumutsi, mwa atumwi anu”. 1 Atesalonika 4:17; “Pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nawo pamodzi m’mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse”.

GAWO LACHIWIRI: ZIMENE TIYENERA KUMACHITA

1. MALAMULO A CHIKHALIDWE

FUNSO 39. Kodi udindo wa munthu kwa Mulungu ndi wotani?

YANKHO. Udindo wa munthu kwa Mulungu ndiye kumvera chifuniro chake.

Mika 6:7; “Kodi Yehova adzakondwera nazo nkhusa zamphongo zikwi khumi? Kodi ndipereke mwana wanga woyamba chifukwa chakulakwa, chipatso cha thupi langa chifukwa cha kuchimwa kwa moyo wanga?”

FUNSO 40. Kodi poyamba Mulungu anaulula chiyani kwa munthu palamulo la kumvera lye?

YANKHO. Mulungu analamula munthu kumvera chilamulo chake.

Aroma 2: 14-15; “Pakuti pamene anthu amitundu akukhala opanda lamulo, amachita mwa okha za

lamulo, omwewo angakhale alibe lamulo, adzakhallira okha ngati lamulo; popeza iwo aonetsa ntchito ya lamulolo yolembedwa m’mitima yao, ndipo chikumbumtima chao chichitiranso umboni pamodzi nawo, ndipo maganizo awo wina ndi mzake anenezana kapena akanirana”.

FUNSO 41. Kodi chilamulo tingachimvetse kuchokera ku chiyani?

YANKHO. Chilamulo tingachimvetse bwino pa malamulo khumi a Mulungu.

Deutronomo 10:4; “Ndipo analembera pagame monga mwa malembedwe oyamba, mawu khumiwo amene Yehova anena ndi inu m’phirimo, ali pakati pa moto tsiku la kusonkhanako ndipo Yehova anandipatsa awa. Mateyu 19: 17; “Ndipo lye anati kwa iye, undifunsiranji za chinthu chabwino? Alipo m’modzi ndiye wabwino, koma ngati ufuna kulowa m’moyo sunga malamulo”.

FUNSO 42. Kodi malamulo khumi amangidwa pa chiyani?

YANKHO. Malamulo khumi amangidwa pa izi: Kukonda Ambuye Mulungu ndi mtima wathu wonse, moyo wathu wonse, mphamvu zathu zonse ndi nzeru zathu zonse ndi kukonda mnzathu monga tidzikondera ife eni.

Mateyu 22:37, 39, 40; “Ndipo Yesu anati kwa iye, uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ndipo lachiwiri lolingana nalo ndi ili: uzikonda mzako monga udzikondera iwe mwini. Pamalamulo awa awiri mpokolowekapo chilamulo chonse ndi aneneri.

FUNSO 43. Kodi mau otsogolera ku malamulo khumi ndi otani?

YANKHO. Mau otsogolera kumalamulo khumi ndi awa: Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakutulutsa iwe kudziko la Aiguputo munyumba ya ukapolo.

Exsodo 20: 2 “Ine ndine Yehova Mulungu wako. Amene ndinatulutsa iwe ku dziko la Aiguputo, kunyumba ya ukapolo.

FUNSO 44. Kodi mawu otsogolera ku Malamulo khumi akutiphunzitsa chiyani?

YANKHO. Mau otsogolera ku Malamulo khumi a Mulungu amatiphunzitsa kuti

popeza Mulungu ndi Ambuye ndi Mulungu wathu ndiponso ndi mombolo wathu, kotero kuti tiri oyenera kusunga malamulo ake onse.

Deutronomo 11:1; “Chifukwa chake mudzikonda Yehova Mulungu wanu, ndi kusunga chilangizo chake, ndi malemba ake, masiku onse” Luka 1: 74-75; “Kutipatsa ife kuti titalanditsidwa ku dzanja la adani athu, tidzamtumikira Iye, opanda mantha. M’chiyero ndi mchilungamo pamaso pake, masiku athu onse.

GAWO LOYAMBA LA MALAMULO

2. LAMULO LOYAMBA

FUNSO 45. Kodi lamulo loyamba ndi lotani?

YANKHO. Lamulo loyamba ndi limene limati: Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha.

FUNSO 46. Kodi mulamulo loyambali akufuna chiyani?

YANKHO. Mulamulo loyambali akufuna ife kudziwa ndi kuvomereza kuti Mulungu Yekha ndiye Mulungu woota ndi Mulungu wathu ndipo timupembedze ndi kumulemekeza Iye moyenera.

1 Mbiri 28:9; “Ndipo iwe Solomo mwana wanga umdziwe Mulungu wa atate wako, umtumikire ndi mtima wangwiro ndi moyo waufulu pakuti Yehova asanthula mitima yonse, nazindikira zolingalira zonse za maganizo. Ukamfunafuna Iye udzampeza, koma ukamsiya Iye adzakusiya kosatha”. Miyambo 3:6; “Umlemekeze m’njira zako zonse, Ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako.”

FUNSO 47. Kodi chimene chikuletsedwa mu lamulo loyamba ndi chiyani?

YANKHO. Mulamulo loyamba chikuletsedwa ndi kukhala kopembedza milungu ina.

Masalimo 14:1; “Wauchitsiru amati mu mtima mwake kulibe Mulungu. Achita zovunda, achita ntchito zonyansa, kulibe wakuchita bwino”. Mateyu 4:10; “Pomwepo Yesu ananena kwa Iye, Choka Satana, pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu udzangwadira, ndipo Iye yekha udzamlambira”. Aroma 1:25; “Amenewo anasandutsa choonadi cha

Mulungu chabodza napembedza natumikira cholengedwa ndi kusiya Wolengayo, ndiye wolemekezeka nthawi yosatha. Amen”.

FUNSO 48. Kodi makamaka tikuphonzira chiyani mulamulo ili loyamba mu mawu oti “Koma Inde Ndekha”?

YANKHO. Mau oti koma Ine ndekha, akutiphonzitsa ife kuti Mulungu amene amaona zonsesakondwera pamene ife tipembedza milungu ina.

Masalimo 44: 20-21; “Tikadaiwala dzina la Mulungu wathu, ndi kutambasulira manja athu kwa mulungu wachilendo, Mulungu sakadasanthula ichi kodi? Pakuti adziwa zinsinsi za mtima.”

3. LAMULO LACHIWIRI

FUNSO 49. Kodi lamulo lachiwiri ndi liti?

YANKHO. Lamulo lachiwiri ndi ili: usadzipangire iwe wekha fano losema kapena chifaniziro chilichonse cha zinthu za mthambo lakumwamba kapena za mdziko lapansi kapena za m’madzi apansi pa dziko; usazipembedzere izo, usazitumikire izo; chifukwa Ine Yehova Mulungu ndiri Mulungu wansanje wakulanga ana chifukwa cha atate awo, kufikira m’badwo wachitatu ndi wachinayi kwa iwo amene akudana ndi Ine; ndikuwachitira chifundo anthu zikwizikwi a iwo amene akondana ndi Ine, nasunga malamulo anga.

FUNSO 50. Kodi mulamulo lachiwiri chikufunika ndi chiyani?

YANKHO. Mulamulo lachiwiri chikufunika ndi kulandira, kutsatira ndi kusunga kwathunthu zonse zokhuza chipembedzo ndi malamulo ake monga mmene Mulungu anasonyezera m’Mawu ake.

Mateyu 28: 20; “Ndikuwaphonzitsa asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansu pano”. Deutronomo 12:32 “Chilichonse ndikuuzani,

muchisamalire kuchichita musamaonjezako kapena kuchepetsako”.

FUNSO 51. Kodi mulamulo lachiwiri chimene chili kuletsedwa ndi chiyani?

YANKHO. Lamulo lachiwiri likuletsa kupembedza Mulungu m’mafano kapena njira ina iliyonseimene siinatchulidwe mu Mawu ake.

Deutronomo 4:15; “Potere dzichenjerani nawo moyo wanu ndithu, popeza simunapenya mafanidwe konse tsikuli Yehova ananena ndi inu m’Horebe, ali pakati pa moto. Kuti mungadziipse ndi kudzipangira fano losema lakunga chifaniziro chiri chonse, mafanidwe a mwamuna kapena mkazi”. Mateyu 15: 9; “Koma andilambira Ine kwachabe, ndi kuphunzitsa maphunzitsa, malangizo a anthu.

FUNSO 52. Kodi ndi mfundo zotani zimene zikupezeka mu lamulo lachiwiri?

YANKHO. Mulamulo lachiwiri mukupezeka mfundo izi kwa ife, umwini wa Mulungu , kwa ife ndi chidwi chimene ali nacho kuchipembedzo chake.

Masalimo 95: 3; “Pakuti Yehova ndiye Mulungu wamkulu ndi mfumu yaikulu yoposa milungu yonse”. Exsodo 34:14; “ Pakuti musalambire Mulungu wina, popeza Yehova dzina lake ndiye Wansanje, ali Mulungu wansanje”.

4. LAMULO LACHITATU

FUNSO 53. Kodi lamulo lachitatu ndi lotani?

YANKHO. Lamulo lachitatu ndi ili: Usatchule dzina la Yehova Mulungu wake pachabe; chifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosachimwa, amene atchula pachabe dzina lakelo.

FUNSO 54. Kodi chikufunika ndi chiyani mu lamulo lachitatu?

YANKHO. Lamulo lachitatu likufuna chiyero ndi ulemu pogwiritsa ntchito dzina la Mulungu, Maudindo ake, Mau ake ndi Ntchito zake.

Masalimo 29:2; “Perekani ulemerero kwa Yehova mwa dzina lake, gwadirani Yehova moyera ndi mokometsetsa”. Mlaliki 5:1; “Samalira phazi lako popita ku nyumba ya Mulungu; pakuti kuyandikira kumvera kupambana kupereka nsembe za zitsiru; pakuti sizizindikira kuti zirikuchimwa”. Yobu 36: 24; “Kumbukira kuti mukuze ntchito zake zimene anaziymbira anthu”.

FUNSO 55. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mu lamulo lachitatu?

YANKHO. Mulamulo lachitatu akuletsa kugwiritsa ntchito mosayenera ndi monyoza chinthu china chirichonse chimene Mulungu adzionetsera Yekha.

Malaki 2:2; “Mukapanda kumvera, mukapanda kuliika mumtima mwana, kupatsa dzina langa ulemerero, ati Yehova wamakamu, ndidzakutumizirani temberero, ndi kutemberera madalitso anu; inde, ndawatemberera kale chifukwa simuliika mu mtima” Mateyu 5:34-35; “ Koma Ine ndinena kwa inu, Musalumbire konse, kapena kuchula kumwamba, chifukwa kuli chimpando cha Mulungu. Kapena kuchula dziko lapansi, chifukwa liri popondapo mapazi ake; kapena kutchula Yerusalemu, chifukwa kuli mzinda wa Mfumu yaikurukuru”.

FUNSO 56. Kodi ndi mfundo yotani imene ikupezeka mulamulo lachitatu?

YANKHO. Mfundo imene ikupezeka mulamuloli ndi yoti ngakhale anthu ophwanya lamuloli angazembe chilango cha anthu, iwo sangazembe chilango chachilungamo cha Ambuye Mulungu wathu.

Deutronomo 28: 58-59; “Mukapanda kusamalira kuchita mau onse a chilamulo ichi olembedwa m’buku ili, kuopa dzina ili la ulemerero ndi loopsa, ndilo YEHOVA MULUNGU WANU; Yehova adzachita miliri yanu ndi ya ana anu ikhale yodabwitsa, miliri yaikulu ndi yokhalitsa, ndi nthenda zoipa ndi zokhalitsa”.

5. LAMULO LACHINAYI

FUNSO 57. Kodi lamulo lachinayi ndi lotani?

YANKHO. Lamulo lachinayi ndi ili: Udzikumbumbikira tsiku la Sabata likhale lopatulika. Mmasiku asanu ndi limodzi

udzigwira ndikumaliza ntchito zako zonse; koma tsiku Lachisanu ndi Chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; Usagwire ntchito iliyonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wa mkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako; chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova anamaliza za kumwamba ndi zapansi, ndi Nyanja, ndi zinthu zili m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika.

FUNSO 58. Kodi chifunika ndi chiyani mulamulo lachinayi?

YANKHO. Mulamulo lachinayi chifunika ndi kusunga chiyero kwa Mulungu ku nthawi zonse zoikika zimene lye wazisankha m'mawu ake; ndikusunga m'masiku asanu ndi awiri kuti likhale Sabata lopatulika kwa lye Yekha.

Levitiko 19:30; "Muzisunga masabata anga, ndikuchitira ulemu malo anga opatulika; Ine ndine Yehova". Deutronomo 5:12; "Samalira lasabata likhale lopaturika monga Yehova Mulungu wako anakulamulira".

FUNSO 59. Kodi ndi tsiku liti mwa masiku asanu ndi awiri limene Mulungu anapatula kuti likhale la Sabata?

YANKHO. Kuchokera pachiyambi cha dziko kufikira kuuka m'manda kwa Yesu Khristu, Mulunguanasankha tsiku lachisanu ndi chiwiri (tsiku Loweruka) kuti likhale Sabata; ndipo atauka Yesu Khristu sabata linasintha kukhala tsiku loyamba la pa Sabata (tsiku la Mulungu), ndipo izi zitsatiridwe mpaka kutha kwa dziko.

Genesis 2:3; "Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri naliyeretsa limenelo chifukwa limenelo adapuma ku ntchito yake yonse imene Mulungu anairenga ndikuyipanga". Machitidwe

20:7; "Ndipo tsiku loyamba lasabata posonkhana ife, kunyema mkate; Paulo anawafotokozeru mawu, popeza anati achoke m'mawa wake ndipo ananena chineneru kufikira pakati pa usiku". Chivumbulutso 1:10; "Ndinagwidwa ndi mzimu Tsiku la Ambuye ndipo ndinamva kumbuyo kwanga mawu akulu ngati a lipenga.

FUNSO 60. Nanga tsiku la Sabata liyenera kuyeretsedwa bwanji?

YANKHO. Tsiku la Sabata liyenera kuyeretsedwa pakupumula mchiyero tsiku lonse lathunthu ngakhalenso ku ntchito zonse za dziko ndi zamasewero zimene timazigwira masiku onse ndikugwiritsa ntchito nthawi yathu yonse mkupembedza Mulungu m'magulu kapena mwamseri, kupatulapo ntchito zofunikira zokha ndi chifundo.

Levitiko 23:3; "Masiku asanu ndi limodzi azigwira ntchito, koma lachisanu ndi chiwiri ndilo sabata la kupumula, msonkhano wopatulika; musagwira ntchito konse; ndilo sabata la Yehova mnyumba zanu zonse". Mateyu 12: 11-12; "Koma lye anati kwa iwo, Munthu ndani wa inu amene ali nkhosa imodzi, ndipo ngati idzagwa mdzenje tsiku la Sabata kodi sadzagwira ndi kuiturutsa? Nanga kuposa nkotani chifukwa cha ichi nkoleleka kuchita zabwino tsiku la Sabata?"

FUNSO 61. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mu lamulo lachinayi?

YANKHO. Mulamulo lachinayi chikuletsedwa ndi kusachita kapena kusasamala pakugwirantchito zoyenera, ndi kuononga tsikuli pa kungokhala kapena kuchita tchimo kapena kukhala ndi maganizo osayenera, m'mawu mu ndi mu ntchito zathu zonse.

Yesaya 58:13-14; "Ukaletsu phazi lako pa Sabata ndi kusiya kuchita kukondwera kwatsiku langa lopatulika, ndi kuyesa Sabata tsiku lokondwa lopatulika la Yehova, lolemekezeka, ndipo ukalilemekeza ilo, osachita njira zako zokha, osafuna kukondwa kwako kokha, osalankhula mawu ako okha; pomwepo udzakondwa mwa Yehova; ndipo Ine ndidzakuyendetsa pa misanje ya dziko lapansi; ndipo ndidzakudyetsa cholowa cha kholo lako Yakokobo; pakuti pakamwa pa Yehova pananenapo." Malaki 1:13; "Kutonso, taonani,

ncholemetsa ichi! Ndipo mwachipeputsa, ati Yehova wa Makamu; ndipo mwabwera nazo zofunkha, ndi zotsimphina, ndi zodwala; momwemo mubwera nayo nsembe; kodi ndiyenera kuilandira kudzanja lanu? Ati Yehova". Ezekeieli 23: 38; "Anandichitiranso ichi, anadetsa malo anga opatulika tsiku lomwelo, naipsa masabata anga".

FUNSO 62. Kodi ndi mfundo zotani zimene zikupezeka mu lamulo lachinayili?

YANKHO. Mfundo zopezeka mu lamulo lachinayi ndi izi: Mulungu akutilola ife masiku asanu ndi limodzi kugwira ntchito zathu zonse, tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi tsiku la Yehova, iye akupereka chitsanzo cha iye mwini, iye akudalitsa tsiku la Sabata.

Eksodo 31:15; "Agwire ntchito masiku asanu ndi limodzi, koma lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata lakupumula, lopatulika la Yehova; aliyense wogwira ntchito tsiku la Sabata aphedwe ndithu". Genesis 2:3; "Mulungu anadalitsa tsiku la chisanu ndi chiwiri naliyetsa limenelo: Chifukwa limenelo anapuma kuntchito yake yonse imene Mulungu anailenga ndi Kupanga.

GAWO LACHIWIRI LAMALAMULO

6. LAMULO LACHISANU

FUNSO 63. Kodi lamulo lachisanu ndi liti?

YANKHO. Lamulo lachisanu ndi ili: Udzilemekeza atate wako ndi amako; kuti achuluke masikuako mu dziko limene Ambuye Yehova Mulungu wako akupatsa iwe.

FUNSO 64. Kodi chikufunikira ndi chiyani mulamulo lachisanu?

YANKHO. Mulamulo lachisanu chikufunikira ndi kusunga ulemu, ndi kuonetsa ntchito zoyenerakwa aliyense molingana ndi udindo wake kaya wachikullire, wachichepere kapenawofanana naye usinkhu.

Akolose 3:20; "Ana inu mverani akubala inu m'zonse, pakuti ichi Ambuye akondwera nacho".

Aefeso 5:21; "Ndi kumverana wina ndi mnzake m'kuopa Khristu".

FUNSO 65. Nanga chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo lachisanu?

YANKHO. Chimene chikuletsedwa mulamulo lachisanu ndi kusapereka ulemu ndikusaonetsantchito zoyenera kwa aliyense molingana ndi udindo wake ndi pamalo ake.

Aroma 13: 7; "Perekani kwa anthu onse mangawa awo; msonkho kwa eni ake ansonkho; kulipira kwa eni ake kulipidwa; kuopa kwa eni ake a kuwaopa; ulemu kwa eni ake a ulemu".

FUNSO 66. Kodi mulamulo limeneli tikupezamo mfundo yotani?

YANKHO. Mfundo yaikulu mu lamulo lachisanu ndi lonjezo la moyo wautali ndi wotukuka kwaanthu onse osunga ilo ndipo ngati atero mu ulemmerero wa Mulungu.

Aefeso 6: 2-3; "Lemekeza atate wako ndi amako (ndilo lamulo loyamba lokhala nalo lonjezano), kuti kukhale bwino ndi iwe, ndi kuti ukhale wa nthawi yaikuru padziko".

7. LAMULO LACHISANU NDI CHIMODZI (6)

FUNSO 67. Kodi lamulo lachisanu ndi chimodzi ndi liti?

YANKHO. Lamulo lachisanu ndi chimodzi ndi ili: Usaphe.

FUNSO 68. Kodi chikufunika ndi chiyani mu lamulo lachisanu ndi chimodzi?

YANKHO. Mulamulo lachisanu ndi chimodzi chimene chikufunika ndi kusunga moyo wathu ndimiyoyo ya anthu ena.

Masalimo 82: 3-4; "Weruzani osauka ndi amasiye; Weruzani molungama ozunzika ndi osowa. Pulumutsani osauka ndi aumphawi; alanditseni m'dzanja la oipa.

FUNSO 69. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo lachisanu ndi chimodzi? YANKHO. Mulamuloli chikuletsedwa ndi kudzychotsera moyo wa ife eni kapena moyo wa m'bale wathu mopanda chilungamo kapena mu njira ina iliyonse.

Machitidwe 16:28; "Koma Paulo anafuula ndi mau aakulu kuti usadzipweteka wekha, tonse tili muno". Mateyu 5:22; "Koma Ine ndinena kwa inu kuti yense wokwiyira mbale wake wopanda chifukwa adzakhala wopalamula mlandu; ndipo amene adzanena ndi mbale wake, Wopanda pake iwe, adzakhala wopalamula mlandu wa akuru: Koma amene adzati, chitsiru iwe: adzakhala wopalamula gehena wamoto".

8. LAMULO LACHISANU NDI CHIWIRI (7)

FUNSO 70. Kodi lamulo lachisanu ndi chiwiri ndi liti?

YANKHO. Lamulo lachisanu ndi chiwiri ndi ili: Usachite chigololo.

FUNSO 71. Kodi chikufunikira ndi chiyani mulamulo lachisanu ndi chiwiri?

YANKHO. Mulamulo lachisanu ndi chiwiri chimene chikufunikira ndi kudziletsa kwa ife eni, kulemekeza umunthu wa anzathu mu mtima, m'malankhulidwe ndi m'makhalidwe.

2 Timoteo 2:22; "Koma thawa zilakolako za unyamata, nusate chilungamo, chikhulupiriro, chikondi, mtendere pamodzi ndi iwo akuitana pa Ambuye ndi mitima yoyera". Aefeso 5: 11-12; "Ndipo musayanjane nazo ntchito za mdima zosabala kanthu, koma makamakanso mudzitsutse. Pakuti zochitidwa mtseri, kungakhale kuzinena kuchititsa manyazi".

FUNSO 72. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mu lamulo lachisanu ndi chiwiri?

YANKHO. Lamulo limeneli likuletsa malingaliro onse oipa, mawu achabe ndi ntchito zonse zosayenera.

Mateyu 5:28; "Koma Ine ndinena kwa Inu, kuti yense wakuyang'ana mkazi kumkhumba, pamenepo watha kuchita naye chigololo mu mtima mwake". Aefeso 5:4; "Kapena zonyasa, ndi

kulankhula zopanda pake, kapena zopusa zimene siziyenera; koma makamaka chiyamiko".

9. LAMULO LACHISANU NDI CHITATU (8)

FUNSO 73. Kodi lamulo lachisanu ndi chitatu ndi liti?

YANKHO. Lamulo lachisanu ndi chitatu ndi ili: Usabe

FUNSO 74. Kodi chikufunika ndi chiyani mu lamulo lachisanu ndi chitatu?

YANKHO. Lamulo lachisanu ndi chitatu likufuna ife kudzipezera chuma ndi katundu wina mu njira yoyenera komanso yachilungamo.

Aefeso 4:28; "Wakubayo asabenso; koma makamaka agwiritse ntchito, nagwire ntchito yokoma ndi manja ake, kuti akhale nacho chakuchereza wosowa. Aroma 12:17; "Musabwezere munthu aliyense choipa. Ganiziranitu zinthu za ulemu pamaso pa anthu onse".

FUNSO 75. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo lachisanu ndi chitatu?

YANKHO. Chimene chikuletsedwa mulamuloli ndi kudzitengera kwa ife tokha chuma kapena katundu wa anzathu mu njira yopanda chilungamo.

Miyambo 28:19; "Wolima munda wake zakudya zidzamkwanira; koma wokhota m'mayendedwe ake adzagwa posachedwa". Machitidwe 20: 35; "Mzinthu zonse ndinakupatsani chitsanzo, chakuti pogwiritsa ntchito, koteru muyenera kuthandiza ofoka ndikukumbuka mau a Ambuye Yesu, kuti anati Yekha, Kupatsa kutidalitsa koposa kulandira". Miyambo 21:6 "Kupata chuma ndi lilime lonama ndiko nkhungu yoyendayenda ngakhale misampha ya imfa".

10. LAMULO LACHISANU NDI CHINAYI (9)

FUNSO 76. Kodi lamulo lachisanu ndi chinayi ndi liti?

YANKHO. Lamulo lachisanu ndichinayi ndi ili: Usamnamizire mzako.

FUNSO 77. Kodi chikufunikira ndi chiyani mulamulo lachisanu ndi chinayi?

YANKHO. Lamulo lachisanu ndi chinayi likutipempha ife kusunga ndi kukweza choonadi pakatipathu ndi kuchitirana umboni.

Zekariya 8:16; “Izi ndizo muzichite; weruzani zooni ndi chiweruzo cha mtendere m’zipata zanu”. Miyambo 14: 5, 25; “Mboni yokhulupirika sidzanama, koma mboni yonyenga imalankhula zonama. Mboni yooni imalanditsa miyoyo; koma wolankhula zonama angonyenga”.

FUNSO 78. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo lachisanu ndichinayi?

YANKHO. Mulamulo lachisanu ndichinayi chimene chikuletsedwa ndi china chilichonse choipitsa choonadi kapena kudziongetsa ife tokha komanso maina abwino a anzathu.

Masalimo 15:3; “Amene sasinjirira ndi lilime lake, sachitira nzake choipa. Ndipo satola mseche pa mnasi wake”. Aroma 3:13; “Mmero mwao muli manda apululu, ndi lilime lawo amanyenga; Ululu wa mamba uli pa milomo yawo”. Aefeso 4:31; “Chiwawo chonse, ndi kupsa mtima, ndi mkwiyo, ndi chiwawa, ndi mwano zichotsedwe kwa inu, ndiponso choipa chonse.

11. LAMULO LAKHUMI

FUNSO 79. Kodi lamulo lakhumi ndi liti?

YANKHO. Lamulo lakhumi ndi limene limati: usasirire nyumba yake ya mzako, usasirire mkazi wake wa mnzako, kapena wantchito wake wa mwamuna, kapena wantchito wake wa mkazi, kapena ng’ombe yake kapena bulu wake, kapena kanthu kalikonse kamzako.

FUNSO 80. Kodi chikufunikira ndi chiyani mulamulo la khumi?

YANKHO. Lamulo la khumi likutiphunzitsa ife kukhala okwanitsidwa ndikukhala ndi mtima wolemekeza katundu wa anthu.

1 Timoteo 6:8; “Koma pokhala nazo zakudya ndi zofunda, zimenezi zitikwanire. Ahebri 13:5; “Mtima wanu ukhale osakonda chuma; zimene muli nazo zikukwanireni; pakuti iye anati, sindidzakusiyi

konse, kungakhale kukutaya, sindidzakutaya ndithu”.

FUNSO 81. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo la khumi?

YANKHO. Lamulo lakhumi likutiletsa ife kukhala osakwanitsidwa pa zinthu zimene tili nazo, kuchitira nsanje kapena kuipidwa ndi zinthu zabwino za anzathu.

Agalatiya 5:26; “Tisakhale odzikuzi, osutsana, akuchitirana njiru”. Luka 12:15; “Ndipo Iye anati kwa iwo, Yang’anirani, mudzisungire kupewa msiriro uliwonse; chifukwa moyo wake wa munthu sulingana ndi kuchuluka kwa zinthu zake ali nazo”.

12. CHILANGO CHOPHWANYA LAMULO LA MULUNGU

FUNSO 82. Kodi pali munthu aliyense amene angasunge mwangwiro malamulo a Mulungu?

YANKHO. Palibe ndi m’modzi yemwe angathe kusunga malamulo a Mulungu mwangwiro m’moyo uno, pakuti munthu amachimwa nthawi ndi nthawi m’magano, m’mawu ndi m’machitidwe.

Mlaliki 7:20; “Pakuti palibe wolungama pansu pano, amene achita zabwino osachimwa”. Masalimo 14:3; “Anapatuka onse; pamodzi anabvunda mtima; palibe wakuchita bwino ndi mmodzi yense”.

FUNSO 83. Kodi machimo ophwanya malamulo a Mulungu ndi ofanana kuopsya kwawo?

YANKHO. Machimo ena ndi oopsya kuposa ena pamaso pa Mulungu.

Luka 12: 47-48; “Ndipo kapolo uyo, wodziwa chifuniro cha Ambuye wake, ndipo sanakonza ndi kusachita zonga za chifuniro chakecho, adzakwapulidwa mikwapulo yambiri. Koma Iye amene sanadziwa, ndipo anazichita zoyenera mikwapulo, adzakwapulikwa pang’ono.

FUNSO 84. Kodi tchimo lililonse limayenera chiyani?

YANKHO. Tchimo lililonse limayenera Mkwiyo ndi Temberero la Mulungu m’moyo uno komanso umene ulikudza.

Aroma 6:23; “Pakuti mphoto yake ya uchimo ndi imfa”. Mateyu 25: 41; “Pomwepo adzanena kwa kwa iwo a ku dzanja lamanzere, Chokani kwa lne otembereredwa inu, ku moto wa nthawi zonse wokolezedwera ndierekezi ndi a mithenga ake”.

13. NJIRA YA CHIPULUPUMUTSO

FUNSO 85. Kodi Mulungu akufuna tichite chiyani kuti tipewe mkwiyo ndi temberero malingana ndi tchimo lathu?

YANKHO. Kuti tipewe mkwiyo ndi temberero malingana ndi machimo athu, Mulungu akufuna ife tikhale ndi chikhulupiriro mwa Yesu Khristu, moyo wakulapa, ndikugwira njira zonse zachionbolo zimene Yesu anatiululira.

Machitidwe 20: 21; “Ndikuchira umboni a Yuda ndi a Helene wa kutembenuka mtima kulinga kwa Mulungu ndi chikhulupiriro cholinga kwa Ambuye wathu.

FUNSO 86. Kodi chikhulupiriro mwa Yesu Khristu ndi chiyani?

YANKHO. Chikhulupiriro mwa Yesu Khristu ndi chisomo cha chipulumutso chathu, chimene timalandira ndi kutsamira pa lye yekha kuti tipulumutsidwe, monga anadziperekerera kwa ife mu uthenga wabwino.

Yohane 3:16; “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi koteru anatuma Mwana Wake Wobadwa Yekha, kuti wokhulupirira lye asataike koma akhale nawo moyo wosatha”. Machitidwe 4:12; “Ndipo palibe chipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansu pathambo lakumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo”.

FUNSO 87. Kodi moyo wakulapa ndi chiyani?

YANKHO. Moyo wakulapa ndi chisomo chopulumutsa chochitika pamene wochimwa wazindikira tchimo lake ndi chifundo cha Mulungu mwa Khristu ndi kumva chisoni ndi kudana ndi tchimo lake, ndikutembenukira kwa Mulungu motsimikizika ndikuyamba kumvera lye.

Luka 13:3; “Ndinena kwa inu, laitu; koma ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo”. Luka 18:13; “Koma wamsonkhoyo alikuima patali sanafuna kungakhale kukweza maso kumwamba, komatu anaziguguda pachifuwa pake nanena, Mulungu, mundichitire chifundo, ine wochimwa”.

FUNSO 88. Kodi ndi njira ziti zime Khristu amationetsera ife ubwino wa chiombolo?

YANKHO. Njira zimene Khristu amationetsera ife ubwino wa chiombolo ndi kudzera m’ Malamulo ake, makakamaka m’ mawu, masakaramenti ndi pemphero; ndipo izi zonse zimagwira ntchito ku chipulumutso cha osankhika.

Machitidwe 2:42; “Ndipo anali chikhaliro m’ chiphunzitsa cha atumwi ndi m’ chianjano, m’ kuniyema mkate ndi mapemphero. 2 Timoteo 3:15; “Ndikuti kuyambira ukhanda wako wadziwa malembo opatulika, okhoza kukupatsa nzeru kufikira chipulumutso, mwa chikhulupiriro cha mwa khristu Yesu”.

14. BUKU LOPATULIKA (BAIBULO) NGATI NJIRA YA CHISOMO

FUNSO 89. Kodi Mau amapangigwa bwanji kukhala ndi mphamvu yopulumutsa?

YANKHO. Mzimu wa Mulungu umapangitsa kuwerenga kwa Mau a Mulungu makamaka ulaliki, kukhala njira yotsimikizika ndiponso yotembenezira ochimwa pakuwaiika iwo mu chiyero ndi muchithonhozo, kupyolera mu chikhulupiriro kufikira ku chipulumutso.

Masalimo 19:7; “Zakumwamba zimalalikira ulemereero wa Mulungu; ndipo thambo lionetsa ntchito ya manja ake”. 2 Timoteo 3:16; “Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitsa, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m’ chipulumutso.

FUNSO 90. Nanga mawu angawerengedwe ndi kumveka bwanji kuti akhale ndi mphamvu yopulumutsa?

YANKHO. Kuti mawuwa akhale ndi mphamvu yopulumutsa tiyenera

kumvetsetsa bwino pokonzekera ndi pemphero, kuwalandira ndi chikhulupiriro ndi chikondi ndi kuwakhazikitsa m’mitima yathu ndikuwagwiritsa ntchito mmoyo wathu.

Masalimo 119:11; “Ndinawabisa mawu anu mu mtima mwanga, kuti ndisalakwire Inu”. Ahebri 4:2; “Pakuti kwa ifenso walalikidwa uthenga wabwino, monganso kwa iwo; koma iwowa sanapindula nawo mau omvekawo, popeza sanasanganizika ndi chikhulupiriro mwa iwo amene adamva”.

15. MASAKARAMENTI NGATI NJIRA YACHISOMO

FUNSO 91. Kodi masakaramenti amakhala bwanji njira yachipulumutso?

YANKHO. Masakaramenti amakhala njira yachipulumutso, osati mwa iwo wokha ayi kapena amene awagwiritsa ntchito iwo, koma ndi mdalitso wa Khristu wokha, ndi ntchito ya Mzimu Woyera mwa iwo amene awalandira ndi chikhulupiriro.

1 Akorinto 3:7; “Chotero Sali kanthu kapena wookayo, kapena wothirirayo; koma Mulungu amene akulitsa”. 1 Akorinto 11:29; “Pakuti iye wakudya ndi wakumwa, adya namwa chiweruziro kwa iye yekha, ngati sazindikira thupilo”. 1 Petulo 3:21; “Chimenechonso chifaniziro chake chikupulumutsani tspano, ndicho ubatizo, kosati kutaya kwa litsiro lake la thupi, komatu funso lake la chikumbumtima chokoma cha Mulungu, mwa kuuka kwa Yesu Khristu”.

FUNSO 92. Kodi Sakaramenti ndi chiyani?

YANKHO. Sakaramenti ndi lamulo loyera lokhazikitsidwa ndi Khristu, limene mukupyolera muzizindikiro zooneka, Khristu ndi ubwino wa Pangano latsopano, zimaonekera, kusindikizidwa ndi kutsatiridwa ndi okhulupirira.

Genesis 17:10; “Ili ndi pangano langa limene uzisunga pakati pa Ine ndi Iwe ndi mbewu zako zapambuyo pako; azidulidwa amuna onse amwa inu”. Aroma 4:11; “Ndipo iye analandira chizindikiro cha mdulidwe, ndicho chosindikiza chilungamo cha chikhulupiriro, chomwe iye anali nacho asanadulidwe; kuti kotero Iye akhale kholo

la onse akukhulupirira, angakhale iwo sanadulidwa, kuti chilungamo chiwerengedwe kwa iwonso”.

FUNSO 93. Kodi masakaramenti a Chipangano Chatsopano ndi ati?

YANKHO. Masakaramenti a Chipangano Chatsopano ndi awa: Ubatizo ndi Mgonero wa Ambuye.

Mateyu 28:19; “Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m’dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera”. Mateyu 26:26; “Ndipo pamene iwo anali kudya, Yesu anatenga mkate, nadalitsa, naunyema; ndipo m’mene anapatsa kwa ophunzira, anati, Tengani, idyani; ichi ndi thupi langa”.

16. UBATIZO

FUNSO 94. Kodi ubatizo ndi chiyani?

YANKHO. Ubatizo ndi sakaramenti limene munthu amatsambitsidwa ndi madzi m’dzina la Atate ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera, chimene chiri chizindikiro cha malowedwe athu kwa Khristu ndi kulandira ubwino wa Chipangano cha Chisomo ndikukhala ake a Ambuye.

Mateyu 28:19; “Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m’dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera”. Aroma 6:3; “Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Khristu Yesu, tinabatizidwa mu imfa yake?”

FUNSO 95. Kodi ubatizo ungaperekedwe kwa yani?

YANKHO. Ubatizo siuyenera kwa munthu wina aliyense amene ali kunja kwa mpingo kufikira atavomereza chikukhulupiriro chawo mwa Khristu ndi kumvera Iye; komanso ana popeza nawonso ali chiwalo cha mpingo, ayenera kubatizidwa.

Machitidwe 2:41; “Pamene iwo amene analandira mawu ake anabatizidwa; ndipo anaonjedzwa tsiku lomwelo anthu ngati zikwi zitatatu (3000)”. Machitidwe 2:39; “Pakuti lonjezani liri kwa inu,, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse akutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana”.

17. Mgonero wa Ambuye

FUNSO 96. Kodi mgonero wa Ambuye ndi chiyani?

YANKHO. Mgonero ndi sakaramenti limene pakupereka ndi kulandira vinyo monga momwe Khristu anachitira, imfa yake imakonetsedwa; ndipo olandirawo sangolandira kuthupi, koma mwachikhulupiriro amadya nawo thupi ndi kumwa mwazi wake ndi ubwino wake wonse, ku moyo wawo wa uzimu ndikukula kwawo mu chisomo.

1 Akorinto 10:16; “Chikho chadalitso chimene tidalitsa, sichiri chijanano cha mwazi wa Khristu kodi? Mkate umene tinyema suli chijanano cha thupi la Khristu kodi?” 1 Akorinto 11: 23; “Pakuti ine ndinalandira kwa Ambuye chimenonso ndinapereka kwa inu, kuti Ambuye Yesu usiku uja anaperekedwa, anatenga mkate...”. Luka 22: 19-20; “Ndipo mmene anatenga mkate, nayamika, anaunyema nawapatsa, nanena, Ichi ndi thupi langa, lopatsidwa chifukwa cha inu; chitani ichi chikumbukiro changa. Ndipo choteronso chikho, atatha mgonero, nanena, Chikho ichi ndi pangano latsopano m’mwazi wanga wothiridwa chifukwa cha Inu”.

FUNSO 97. Kodi chikufunika ndi chiyani kwa iwo oyenera kulandira mgonero wa Ambuye?

YANKHO. Chofunika kwa iwo oyenera kulandira mgonero wa Ambuye ndi kuti adziyese okha mu nzeru zawo pakuzindikira thupi la Ambuye, chikhulupiriro chawo, kulapa kwawo, chikondi ndi kumvera kwatsopano, poopa kuti ngati ali osayenera, akhoza kudziitanira mkwiyo wa Mulungu kwa iwo eni.

1 Akorinto 11: 28-29; “Koma munthu adziyese yekha, ndikotero adye mkate, ndikumwera chikho. Pakuti iye wakudya, adya namwa chiweruziro kwa yekha, ngati sazindikira thupilo”. 1 Akorinto 5:8; “Chifukwa chake tichita phwando sindichotupitsa chakale, kapena ndi chotupitsa cha dumbo ndi kuipa mtima, koma ndi mkate wosatupa wa kuona mtima ndi choonadi”.

18. Pemphero ngati njira Yachisomo

FUNSO 98. Kodi pemphero ndi chiyani?

YANKHO. Pemphero ndikupereka zokhumba zathu kwa Mulungu ku zinthu zovomerezeka ndi chifuniro chake mu dzina la Khristu, ndi pakulapa machimo athu ndi kuvomereza koyamika chifundo chake.

Mateyu 7:7; “Pemphani ,ndipo chidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo chidzatsogolidwa kwa inu”. Yohane 16: 23; “Indetu , Indetu ndinena kwa inu, ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu mu dzina langa”. Afilipi 4:6; “Musadere nkhwaka konse, komatu muzonse ndipemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu”.

FUNSO 99. Kodi ndi lamulo lotani limene Mulungu wapereka lotitsogolera ku pemphero?

YANKHO. Mau onse a Mulungu a m’Bukhu Lopatulika ndiwo atitsogolera ife m’pemphero; komonso pali lamulo lapadera limene Khristu anaphunzitsa ophunzira ake, limene litchedwa Pemphero la Ambuye.

1 Yohane 5:14; “Ndipo uku ndikulimbika mtima kumene tiri nako kwa Iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa chifuniro chake, atimvera”. Mateyu 6:9; “Chifukwa chake pempherani inu chomwechi: Atate wathu wa Kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe,”.

19. Pemphero la Ambuye

FUNSO 100. Kodi mau oyambirira pa pemphero la Ambuye amatiphunzitsa ife chiyani?

YANKHO. Mau oyambirira a pemphero la Ambuye oti: Atate wathu wakumwamba, amatiphunzitsa ife kusendeza chifupi ndi Mulungu mkudzichepetsa konse, mchiyero ndi chitsimikizo monga ana kwa atate wawo, okhoza kutithandiza ife,

ndikuti tikhoza kudzipempherera tokha ndikupemphereranso anzathu.

Mateyu 6:9; “Chifukwa chake pempherani inu chomwechi: Atate wathu wa Kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe,”. Aroma 8:15; “Pakuti inu simunalandira mzimu waukapolo, kuchitanso mantha, koma munalandira Mzimu wa umwana umene tifuula kuti Abba, Atate”.

FUNSO 101. Kodi timapempherera chiyani mugawo loyamba?

YANKHO. Mugawo loyamba (limene liri: Dzina Lanu Liyeretsedwe)timapempha Mulungu kuti atipangitse ife ndi anzathu kumulemekeza lye mu zonse zimene amazonetsera; kuti atiwonetse ulemerero wake ku zinthu zake zonse.

Masalimo 67: 3 “Anthu akuyamikeni, Mulungu; Anthu onse akuyamikeni. Aroma 11:36; “Chifukwa zinthu zonse zichokera kwa lye, zichitika mwa lye ndikufikira kwa lye, kwa lye kukhale ulemerero kunthawi zonse. Amen”.

FUNSO 102. Kodi timapempherera chiyani mu chigawo chachiwiri?

YANKHO. Muchigawo chachiwiri (chimene chiri: Ufumu Wanu Udze), timapempherera kuti ufumu wa Satana uwonongedwe; ndi kuti ufumu wa chisomo ukudzidwe mwa ife ndi ena otengedwa nawo momwemu, ndi kuti ufumu wa ulemerero ufulumizidwe.

Masalimo 68:1; “Auke Mulungu, abalalike adani ake; Iwonso akumuda athawe pamaso pake”. Masalimo 51:18; “Chitirani Ziyoni chokoma monga mwa kukondwera kwanu, mumange malinga a miyala a Yerusalemu”. Chibvumbulutsa 22: 20; “Iye wakuchitira umboni izi, anena, Indetu ndidza nsanga Ameni; Idzani Ambuye Yesu”.

FUNSO 103. Kodi timapempherera chiyani mu chigawo chachitatu?

YANKHO. Muchigawo chachitatu (chimene chiri: Kufuna kwanu kuchitidwe monga kumwamba chomwecho pansi pano), timapempherera kuti Mulungu mwa chisomo chake atipangitse ife kudziwa, kumvera, ndi kugonjera ku

chifuniro chake mu zinthu zonse, monga alikuchitira angelo kumwamba.

Masalimo 119:34; “Mundizindikiritse, ndipo ndidzasunga malamulo anu; Ndidzawasamalira ndi mtima wanga wonse”. Mateyu 26: 39; “Ndipo anamuka patsogolo pang’ono, nagwa nkhope yake pansi, napemphera nati, Atate ngati nkutheka, chikho ichi chindipitirire Ine; koma simonga ndifuna Ine koma Inu.

FUNSO 104. Kodi timapempherera chiyani mu chigawo chachinayi?

YANKHO. Muchigawo chachinayi (Chimene chiri: Mutipatse ife chakudya chathu chalero) timapempherera kuti: Kuchokera mu mphatso yaulere ya Mulungu, tilandireko gawo la zinthu zabwino m’moyo uno, ndi kukondwera ndi madalitso ake.

Miyambo 30:8; “Mundichotsere kutali zachabe ndi mabodza; musandipatse umphawi ngakhale chuma, mundidyetse zakudya zondiyenera”. Masalimo 90:17; “Ndipo chisomo chake cha Yehova Mulungu wathu chikhale pa ife. Ndipo mutikhazikitsire ife ntchito ya manja athu, inde ntchito ya manja athu muikhazikitse”.

FUNSO 105. Kodi timapempherera chiyani muchigawo chachisanu?

YANKHO. Muchigawo chachisanu (Chimene chiri: Ndipo mutikhululukire ife zochimwa zathu monga ifenso tiwakhululukira amangawa athu) timapemphelera kuti Mulungu mwa Khristu, atikhululukire zochimwa zathu; zomwe ife tikukakamizidwa kupempha, chifukwa mwa chisomo chake ife tili kuloledwa kukhululukira anzathu kuchokera pansi pa mtima.

Masalimo 51:1; “Mundichitire ine chifundo Mulungu, monga mwakukoma mtima kwanu, monga mwa unyinjira wa nsoni zokoma zanu mufafanize machimo anga”. Mateyu 6: 14; “Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zawo, adzakhululukira inunso Atate wanu wakumwamba”.

FUNSO 106. Kodi timapempherera chiyani muchigawo chachisanu ndi chimodzi?

YANKHO. Muchigawo chachisanu ndi chimodzi (Chimene chiri: Musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse ife kwa woipayo), timapempherera kuti Mulungu atichinjirize ife ku mayesero a uchimo, kapena kutithandiza kutilanditsa ife pamene tiyesedwa.

Mateyu 26: 41; “Chezerani ndi kupempherera kuti mungalowe mkuyesedwa; Mzimutu uli wakufa koma thupi liri lolefuka”. Masalimo 19:13; “Ndiponso muletse kapolo wanu pa zodzitama; zisachite ufumu pa ine: pamenepo ndidzakhala wangwiro, ndiwosachimwa cholakwa chachikuru.

FUNSO 107. Kodi kutsiriza kwa pemphero la Ambuye kumatiphunzitsa ife chiyani?

YANKHO. Matsiriziro a pemphero la Ambuye (amene ali: Pakuti wanu uli ufumu

ndi mphamvu ndi ulemerero, wanthawi zonse Amen) , akutiphunzitsa ife kukhala ndi chilimbikitso mu pemphero la Ambuye lokha basi; ndi m’mapemphero athu olemekeza iye, potchula ufumu, mphamvu ndi ulemerero kwa Iye. Ndipo pakuchitira umboni pakhumbo lathu, chi chitsimikizo chofuna kumvetseredwa, tikuti Amen.

1 Mbiri 29:11,13; “Ukulu ndi mphamvu ndi ulemelero ndi kulakika, ndi chifumu ndi zanu Yehova; pakuti zonse zam’mwamba ndi pa dziko lapansi ndi zanu; ufumu ndi wanu, Yehova; ndipo mwakwezeka mutu wa pa zonse. Motero tsono, Mulungu wathu, tikuyamikani ndi kulemekeza dzina lanu lokoma”. Masalimo 106:48; “Ndi anthu onse anene, Amen”. Chibvumbulutso 22:20; “Iye wakuchitira umboni izi anena indetu ndidza nsanga. Amen idzani Ambuye Yesu”.

MAFUNSO OBWEREZA:

KUDZIWA MAYANKHO A MAFUNSO ONSEWA (107) KUTHANDIZA KUTI MOYO WANU WA UZIMU UKHALE WOZAMA NDI WOKHAZIDKIKA. PAJA MAU AKUTI ANTHU ANGA AKUONONGEKA CHIFUKWA CHOSADZIWA. INU KHALANI ODZIWA KUTI MUSAONONGEKE!

1. Cholinga chenicheni chimene munthu ayenera kuchita kwa Mulungu ndi chiyani?
2. Kodi ndi lamulo liti lomwe Mulungu wapereka lotitsogolera ife m’mwene tingamlemekezere ndi kukondwerera mwa Iye?
3. Kodi mawu a Mulungu kwenikweni amaphunzitsa chiyani?
4. Kodi Mulungu ndi ndani?
5. Kodi ilipo Milungu inanso?
6. Kodi mu Umulungu muli anthu angati?
7. Kodi malamulo a Mulungu ndi otani?
8. Nanga Mulungu akukwaniritsa bwanji malamulo ake?
9. Kodi ntchito ya chilengedwe ndi yotani?
10. Kodi munthu analengedwa bwanji?
11. Kodi ntchito za Mulungu muchisamaliro chake ndi zotani?
12. Kodi ndi chisamaliro chapadera chotani chimene Mulungu anaonetsera kwa munthu m’manda umene analengedwera?
13. Kodi makolo anthu oyamba anapitilira kukhalabe m’mene adalengedwera?
14. Kodi tchimo ndi chiyani?

15. Kodi ndi tchimo lanji limene linapangitsa makolo athu oyamba kugwa kuchokera m'manja mwa Mulungu?
16. Kodi mtundu wonse wa anthu unachimwanso pamene Adamu anachimwa koyamba?
17. Nanga kugwa kwa Adamu kunabweretsa chiyani ku mtundu wa anthu?
18. Kodi tchimo limene linafikira munthu limapezeka mu chiyani?
19. Kodi ndi masautso otani amene anabwera kwa munthu chifukwa cha uchimo?
20. Kodi Mulungu analekelera mtundu wa anthu kuti uwonongeke m'machimo ndi m'masautso awo?
21. Kodi Mpulumutsi wa anthu osankhidwa a Mulungu ndi ndani?
22. Kodi Khristu pokhala mwana wa Mulungu anakhala bwanji munthu?
23. Kodi ndi maudindo ati amene Khristu ali nawo monga mombolo wathu?
24. Kodi Khristu akugwira bwanji ntchito yake ya Uneneri?
25. Kodi Khristu amagwira bwanji ntchito yake ya unsembe?
26. Nanga Khristu anakwaniritsa bwanji udindo wake monga mfumu?
27. Kodi kudzichepetsa kwa Khristu kunali kotani?
28. Kodi kupambana kwa Yesu kunali kotani?
29. Kodi timatenga nawo gawo bwanji ku chiwombolo chimene Khristu anatibweretsa?
30. Kodi Mzimu Woyera amatibweretsa bwanji chiwombolo cha Khristu?
31. Kodi maitanidwe enieni ndi chiyani?
32. Kodi pali phindu lanji limene oitanidwa amapeza mmoyo uno?
33. Kodi kulungamitsidwa ndi chiyani?
34. Kodi kukhala mwana wa Mulungu kukuthanthauza chiyani?
35. Kodi chiyeretso ndi chiyani?
36. Kodi ndi phindu lanji ku moyo uno limene limabwera chifukwa cha kulungamitsidwa, kukhala mwana wa Mulungu, ndi kuyeretsewa?
37. Kodi ndi phindu lanji limene okhulupirira amalandira kuchokera kwa Khristu akamwarira?
38. Kodi ndi phindu lanji limene okhulupirira adzalandira pa tsiku lamdzukiro?
39. Kodi udindo wa munthu kwa Mulungu ndi wotani?
40. Kodi poyamba Mulungu anaulula chiyani kwa munthu palamulo la kumvera lye?
41. Kodi chilamulo tingachimvetse kuchokera ku chiyani?
42. Kodi malamulo khumi amangidwa pa chiyani?
43. Kodi mau otsogolera ku malamulo khumi ndi otani?
44. Kodi mawu otsogolera ku Malamulo khumi akutiphunzitsa chiyani?
45. Kodi lamulo loyamba ndi lotani?
46. Kodi mulamulo loyambali akufuna chiyani?
47. Kodi chimene chikuletsedwa mu lamulo loyamba ndi chiyani?
48. Kodi makamaka tikuphunzira chiyani mulamulo ili loyamba mu mawu oti "Koma Inde Ndekha"?
49. Kodi lamulo lachiwiri ndi liti?
50. Kodi mulamulo lachiwiri chikufunika ndi chiyani?
51. Kodi mulamulo lachiwiri chimene chili kuletsedwa ndi chiyani?

52. Kodi ndi mfundo zotani zimene zikupezeka mu lamulo lachiwiri?
53. Kodi lamulo lachitatu ndi lotani?
54. Kodi chikufunika ndi chiyani mu lamulo lachitatu?
55. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mu lamulo lachitatu?
56. Kodi ndi mfundo yotani imene ikupezeka mulamulo lachitatu?
57. Kodi lamulo lachinayi ndi lotani?
58. Kodi chifunika ndi chiyani mulamulo lachinayi?
59. Kodi ndi tsiku liti mwa masiku asanu ndi awiri limene Mulungu anapatula kuti likhale la Sabata?
60. Nanga tsiku la Sabata liyenera kuyeretsedwa bwanji?
61. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mu lamulo lachinayi?
62. Kodi ndi mfundo zotani zimene zikupezeka mu lamulo lachinayili?
63. Kodi lamulo lachisanu ndi liti?
64. Kodi chikufunikira ndi chiyani mulamulo lachisanu?
65. Nanga chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo lachisanu?
66. Kodi mulamulo limeneli tikupezamo mfundo yotani?
67. Kodi lamulo lachisanu ndi chimodzi ndi liti?
68. Kodi chikufunika ndi chiyani mu lamulo lachisanu ndi chimodzi?
69. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo lachisanu ndi chimodzi?
70. Kodi lamulo lachisanu ndi chiwiri ndi liti?
71. Kodi chikufunikira ndi chiyani mulamulo lachisanu ndi chiwiri?
72. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mu lamulo lachisanu ndi chiwiri?
73. Kodi lamulo lachisanu ndi chitatu ndi liti?
74. Kodi chikufunika ndi chiyani mu lamulo lachisanu ndi chitatu?
75. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo lachisanu ndi chitatu?
76. Kodi lamulo lachisanu ndi chinayi ndi liti?
77. Kodi chikufunikira ndi chiyani mulamulo lachisanu ndi chinayi?
78. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo lachisanu ndichinayi?
79. Kodi lamulo lakhumi ndi liti?
80. Kodi chikufunikira ndi chiyani mulamulo la khumi?
81. Kodi chikuletsedwa ndi chiyani mulamulo la khumi?
82. Kodi pali munthu aliyense amene angasunge mwangwiro malamulo a Mulungu?
83. Kodi machimo ophwanya malamulo a Mulungu ndi ofanana kuopsya kwawo?
84. Kodi tchimo lirilonse limayenera chiyani?
85. Kodi Mulungu akufuna tichite chiyani kuti tipewe mkwiyo ndi temberero malingana ndi tchimo lathu?
86. Kodi chikhulupiro mwa Yesu Khristu ndi chiyani?
87. Kodi moyo wakulapa ndi chiyani?
88. Kodi ndi njira ziti zime Khristu amationetsera ife ubwino wa chiombolo?
89. Kodi Mau amapandigwa bwanji kukhala ndi mphamvu yopulumutsa?
90. Nanga mawu angawerengedwe ndi kumveka bwanji kuti akhale ndi mphamvu yopulumutsa?
91. Kodi masakaramenti amakhala bwanji njira yachipulumutso?
92. Kodi Sakaramenti ndi chiyani?

93. Kodi masakaramenti a Chipangano Chatsopano ndi ati?
94. Kodi ubatizo ndi chiyani?
95. Kodi ubatizo ungaperekedwe kwa yani?
96. Kodi mgonero wa Ambuye ndi chiyani?
97. Kodi chikufunikandi chiyani kwa iwo oyenera kulandira mgonero wa Ambuye?
98. Kodi pemphero ndi chiyani?
99. Kodi ndi lamulo lotani limene Mulungu wapereka lotitsogolera ku pemphero?
100. Kodi mau oyambirira pa pemphero la Ambuye amatiphunzitsa ife chiyani?
101. Kodi timapempherera chiyani mugawo loyamba?
102. Kodi timapempherera chiyani mu chigawo chachiwiri?
103. Kodi timapempherera chiyani mu chigawo chachitatu?
104. Kodi timapempherera chiyani mu chigawo chachinayi?
105. Kodi timapempherera chiyani muchigawo chachisanu?
106. Kodi timapempherera chiyani muchigawo chachisanu ndi chimodzi?
107. Kodi kutsiriza kwa pemphero la Ambuye kumatiphunzitsa ife chiyani?

AMBUYE APITIRIZE KUDALITSA EVANGELICAL PRESBYTERIAN CHURCH (EPC)
KUTI MAMEMBALA AKE ONSE ONSE AKHALE OCHITA MAU ANU MPAKA
KUBWERA KWANU KWA CHIWIRI. ZIKOMO CHIFUKWA CHA MPINGO WATHU
UMENENE UKUTSATIRA MAU ANU.